


# Chekeni ndi Baibulo 2026

GBV

# Januware

## Pakuti monga mvula itsika... [kuti] kuthirira dziko lapansi ..., momwemo adzakhala mawu Anga amene atuluka mkamwa Mwanga.

Baibulo – Yesaya 55:10-11



Mbewu zimafunikira madzi kuti zikule. Popanda madzi, zimawuma. Mofananamo, Mawu a Mulungu amagwira ntchito mwa ife ndi ena tikamawamva kapena kuwauza ena. Kumbukira mavesi a m'Baibulo omwe umawerenga kapena kumva - amakupatsa mphamvu komanso kulimba mtima pa moyo watsiku ndi tsiku. Ukhozanso kugawana ndi ena.


1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31

# Amene ali ndi makutu akumva amve!

Baibulo – Mateyu 11:15

## Feburuware

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28



Agwape ali ndi makutu awo oyimilira.
Kodi akumvetsera chiyani chinthu chofunika?

Mulungu amafunanso kukuuza iwe zinazake, chifukwa amakukonda kwambiri. Anakulemberanso kalata! Ndilo Baibulo. Werenga, kapena pempha wina kuti akuwerengere kuti umve zimene Mulungu akufuna kukuuza zokhudza Iyeyo komanso za iweyo.

# Marichi

# Imani chilili ndi kulingalira zodabwiza za Mulungu.

Baibulo –
Yobu 37:14b




Tayang'ana chilengedwe chakuzungulira ndi kudziyang'anira wekha. Mulungu anapanga zonsezi ndipo amazitcha kuti chilengedwe Chake. Sizinakhaleko zokha chifukwa chakuti chinthu chokongola kwambiri ndi chogwira ntchito mwangwiro sichinachitike mwangozi, ngakhale patapita nthawi yaitali mosadziwika bwino. Mulungu ndi wamphamvu – wamphamvu kwambiri, choncho zindikira zimenezo!

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31

# Epulo

**Khala wamphamvu, nulimbike mtima; usaope, kapena kutenga nkhawa, pakuti Yehova Mulungu wako ali nawe kulikonse umukako.**

Baibulo – Yoswa 1:9



Kodi nthawi zina unamvapo kuti uli wekha? Mwina palibe aliyense pafupi nawe amene umamudziwa bwino. Umasowa mtendere komanso ndi mantha pang'ono.

Kumbukira, siuli wekha. Mulungu ali ndi iwe nthawi zonse ndipo amakuyang'anira. Pemphera kwa Iye ndi kumupempha kuti akuthandize kuti usachite mantha.

Ndithu, adzachita.


1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30

# Ndipo Yehova Mulungu anaitana Adamu nati kwa iye, Uli kuti?

Baibulo – Genesis 3:9

## Meyi

1 2 3 4 5 6 7 8 9 10 11 12 13 14 15 16 17 18 19 20 21 22 23 24 25 26 27 28 29 30 31



Kanyani kakang'ono kamaoneka ngati kakufuna kubisala. Kodi unayamba wabisalapo chifukwa chakuti unachita cholakwika ndipo umkawopa kuti anthu angakupeze? Mulungu akukuitana. Safuna kukuchitira zoipa koma kukukhululukira. Umuwuze Iye moona mtima kuti pepani, ndipo siwudzafunikanso kubisala.

# Juni



Yamikani Yehova, pakuti Iye ndiye wabwino; Pakuti chifundo chake mchosatha.

Baibulo – 1 Mbiri 16:34

M'miyoyo yathu, pali masiku abwino ndi oipa. Pa masiku abwino, n'zosavuta kuthokoza Mulungu. Koma pamasiku achisoni kapena osungulumwa, zimakhala zovuta. Zili ngati dzuwa ndi mitambo. Dzuwa limawala nthawi zonse, ngakhale mitambo ikaphimba. Kumbukirani:

Mulungu ndi wabwino - nthawi zonse!

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30

# Julaye

## Ife tonse tasokera ngati nkhosa; ife tapatuka aliyense m'njira yake.

Baibulo – Yesaya 53:6

Kodi unayamba watsutsanapo, kunama kapena kusamvera? Tonsefe timachita zinthu zimenezi chifukwa ndife ngati nkhosa zimene zathawa Mulungu. Mulungu ayenera kulanga cholakwa chilicohnse, koma Mwana wake, Yesu Kristu, anabwera padziko lapansi ndipo analangidwa pa mtanda chifukwa cha zolakwa zathu.

Ngati upemphera kwa Iye, kuvomereza moona mtima zolakwa zako, ndi kumukhulupirira Iye ndi mtima wako wonse, adzakukhululukira ndi kukutsogolera panjira yabwino.




1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31

Kodi chilengedwe sichodabwitsa? Mulungu amaonetsa kupyolera mu icho kuti Iye akhoza kuchita chirichonse ndipo amalingalira chirichonse. Kupusa kotani nanga kukhulupirira kuti chilengedwe chonse chinangokhalako chokha.

Mulungu adalenga njovu - ndipo iwe ndi ine. Ungathe kudalira Iye kuti iye adzakuthandiza ndi kusamalira chilichonse m'moyo wako. Amakukonda!

# Ogasiti

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31



**Ntchito zanu mzodabwitsa ;**
**Moyo wanga uchidziwa ichi bwino.**

Baibulo – Salmo 139:14b

# Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.

Baibulo – Genesis 1:1

## Sepitembara

Mulungu ndi wamphamvu kwambiri. Iye analenga kumwamba, dziko lapansi, nyama zonse, ndi anthunso. Ngakhale sitingathe kumuwona Iye, Ali paliponse ndipo amayang'anira zomwe adazipanga. Iye amakuonanso. Ukhoza kumukhulupirira Iye kuti adzakuthandiza iwe pa vuto lililonse limene ungakumane nalo.




1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30

# Okutobara

Inu wamaso osalakwa, osapenya zoipa;

Baibulo – Habakuku 1:13a




Ndime iyi ikunena za Mulungu. Tsoka ilo, nthawi zina timachita zinthu zolakwika, monga kunama kapena kusamvera, chifukwa mitima yathu si yoyera. Ndi chifukwa chake talekanitsidwa ndi Mulungu. Koma Mulungu amatikonda kwambiri iwe ndi ine ndipo amafuna kuti tikhale oyera. Sitingathe kuchita tokha. Werenga tsamba lomaliza la kalendalayi - likukuuza momwe Mulungu anamangira mlatho kuti tibwere kwa Iye.

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31

# Novembara

**Ngati wina ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; Zakale zapita; tawonani, zakhala zatsopano.**

Baibulo – 2 Akorinto 5:17



Mbalame yoluka imamanga chisa chatsopano pamene chakalecho chawonongeka. Simakonza koma imapanga chatsopano.

Ifenso, timasweka ndi uchimo, monga kunama kapena maganizo oipa. Ngati ukhulupilira mwa Yesu ndikuulula machimo ako kwa Iye, samangokukonza – amapanga chinthu china chatsopano.


1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30

# Tiyeni tibwerere kumka kwa Yehova.

Baibulo – Hoseya 6:1a


# Disembara

1
2
3
4
5
6
7
8
9
10
11
12
13
14
15
16
17
18
19
20
21
22
23
24
25
26
27
28
29
30
31



Mulungu akutiyembekezera ife ndi manja otsegula. Iye akufuna kuti ife tibwere kwa Iye. Ndi chifukwa chake wachita zonse kuti zitheke. Mwana wake, Yesu Khristu, analandira chilango chifukwa cha maganizo ndi zochita zathu zolakwika pamene anafa pa mtanda. Kudzera mu izi, Mulungu akukuitana lero kuti ubwere kwa Iye. Landira kuyitana Kwake!

# KULEKANITSIDWA NDI MULUNGU



Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulunguwanu;
ndipo machimo anu abisa nkhope yache kwa inu, kuti Iye sakumva.
Baibulo – Yesaya 59:2

Mulungu ndi wabwino – palibe cholakwika kapena choyipa mwa Iye. Ife mwa njira yina timagwiritsa ntchito mau a mwano, timakhala ndi nsanje, kusamvera, kapena kuwachitira mwano anthu ena. Mulungu amazitchula zonsezi tchimo.


Tchimo lapanga mpata, kulekanitsidwa ndi Mulungu. M'mene tiliri sizili bwino ndi Mulungu. Tchimo ndi – monga ngati mu chithunzi – dzenje lalikulu ili pakati pa iwe ndi Mulungu.



Sitikwanitsa kuwoloka "dzenje ili la tchimo" pa ife tokha. Chiyani tsopano? Palibe wina amene angagonjetse dzenje limeneli? Palibe mulatho pakati pa ife ndi Mulungu? Inde, ulipo!

Mulungu Iye mwini anatimangira ife mulatho uwu chifukwa Mulungu amatikonda ife anthu. Mwachikondi, Iye anatumiza mwana wake yekhayo – Yesu Khristu – kukhala mulatho uwu kwa Mulungu.


Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi,
kotero kuti anapatsa mwana wake wokondedwa yekhayo.
Baibulo – Yohane 3:16



Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi choonadi, ndi moyo.
Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine.
Baibulo – Yohane 14:6

Yesu Khristu analangidwa chifukwa cha zoipa zimene mwachita. Ichi ndi chimene Iye anakhalira njira kwa Mulungu. Komabe, mukuyenera kupita ndi njira iyi kuti mudumphe dzenje ili.

Ichi chimatheka bwanji? – khulupirira kuti Ambuye Yesu anafa chifukwa cha machimo ako pa mtanda. Muuze machimo ako ndipo upepese. Mupemphe Ambuye Yesu kuti akukhululukire iwe ndi machimo ako. Kenako Iye adzakupulumutsa iwe ndipo iyi ikhala njira ya iwe pamwamba pa mulatho uwu kwa Mulungu. Yesu akudikira iwe ndipo adzasangalala kwakukulu ngati ubwera kwa iye.



Ngati tibvomereza machimo athu,ali wokhulupirika ndi wolungama iye kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kuti chotsela chosalungama chiri chonse.
Baibulo – 1 Yohane 1:9

Ukangopanga ichi ndipo wawoloka mulatho, Mulungu adzakulandira iwe. Ndipo ukhoza kulankhulakwa iye pa nthawi zonse, ndiwe wopulumutsidwa ndipo chilichonse ndi chilibwino pakati pa Mulungu ndi iwe!

# MOYO NDI MULUNGU




**GBV Dillenburg GmbH**
Eiershäuser Straße 54
35713 Eschenburg
**GERMANY**
www.gbv-dillenburg.de
www.gbv-online.org
www.bibleo.org



CALA christian aid & literature africa
calamalawi@gmail.com
www.biblecenter-mw.com
P.O. Box 30809, Lilongwe 3, **MALAWI**
phone: +265 99 908 1100 | +265 99 613 1252
phone: +265 88 827 4309 | +265 88 559 9473


## Visit our Bible Centers in

**Lilongwe:** Upland House, opposite Maula Mall, Area 3
**Limbe:** Opposite Limbe Police, Building No.2, after Puma filling station, From Illovo Round about.
**Dowa:** Gospel Hall, close to Dzaleka school
**Mzuzu:** Close to Dynapham shop, right turn from SOSOSO bus depot to Mzuzu bus depot


© Grafik: Lydia Jesuthasan



ISBN 978-3-98824-322-5



© 2025 by GBV
printed in Germany



Kumasulira Baibulo: Malemba atengedwa kuchokera mu Baibulo la Buku Lopatulika ® Copyright © 2014 Bible Society of Malawi Agwiritsidwa ntchito ndi chilolezo. Maumwini onse ndi otetezedwa.



GBV 895 7820 Crayon and Bible Chichewa